Baibulo ya ana
Ikupasilani

Mtsogoleri wa Kachisi Akuyendera Yesu

Yolembedwa ndi: Edward Hughes

Yojambulidwa ndi: Byron Unger; Lazarus Alastair Paterson

Yotengedwa ndi: M. Maillot; Sarah S.

Yotathauzidwa ndi: Tapiwa Maraira

Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

©2022 Bible for Children, Inc.
Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.


Tsiku lina Yesu atapita ku Nyumba ya Mulungu, anapeza anthu akunyozetsa Nyumba ya Mulungu. Anali kugulitsa nyama ndi kusinthana ndalama m'Kacisi!

Popanga mkwapulo wa zingwe, Yesu anathamangitsa ogulitsawo m'Kacisi. "Chotsani izi," Iye analamula. "Musamapange Nyumba ya Atate wanga kukhala malo a malonda." Yesu ankakonda Nyumba ya Atate wake.



Atsogoleriwo anapempha chizindikiro chosonyeza kuti Yesu anali ndi ufulu wochotsa Nyumba ya Mulungu. "Pasulani kachisi uyu, ndipo ine ndidzamuwutsa m'masiku atatu," Yesu anayankha. N'zosatheka! Kachisi anatenga zaka makumi anayi ndi zisanu ndi chimodzi kuti amange.

Koma Yesu analankhula za thupi lake. Monga Kachisi, thupi lake linali malo okhalamo Mulungu. Ngakhale kuti Yesu adzafa pamtanda anadziwa kuti Mulungu adzamuukitsa kwa akufa pa tsiku lachitatu.



Usiku, mmodzi wa atsogoleri a pakachisi anapita kwa Yesu. Iye ankadziwa mwa zozizwitsa kuti Yesu anatumidwa ndi Mulungu. Nikodemo anadza kwa Yesu kuti aphunzire zambiri za Mulungu.

Yesu anauza Nikodemo kuti anthu ayenera kubadwanso kuti alowe mu Ufumu wa Mulungu. Nikodemo sanamvetse. Kodi zingatheke bwanji kuti munthu wamkulu akhalenso khanda? Komanso, iye anali wachipembedzo. Kodi zimenezo sizinali zokwan.

“Chobadwa mwa mzimu chikhala mzimu,” Yesu anafotokoza motero. “Mzimu wa Mulungu uli ngati mphepo. Anthu saona mphepo kapena kuimvetsa. Amangoona zimene mphepo imachita.”

Yesu anakumbutsa Nikodemo za ana a Israyeli amene anadandaula kwa Mose kalekale. “Tilibe chakudya, tiribe madzi, ndipo timada mkate umene Mulungu amatipatsa,” iwo anafuula motero.

Uchimo wa anthu unakwiyitsa Mulungu. Anatumiza njoka zamoto pakati pawo. Njoka zinaluma anthu. Ambiri anafa.

“Tachimwa. Pempherani kuti Yehova achotse njoka,” anthu anapempha motero. Chotero Mose anawapempherera. Koma Mulungu sanachotse njokazo.

Mulungu anauza Mose kuti apange njoka yamoto n'kuiika pamtengo. "Aliyense wolumidwa adzakhala ndi moyo ayang'ana njoka pamtengo," analonjeza motero Mulungu. Mose anapanga njoka yamkuwa ndipo amene anaiyang'ana anachiritsidwa.

Yesu anapereka Nidemo kuti Mwana wa munthu
wogwiritsa ntchito kukweza m'mwambamwamba ndi kutsogolo yamkuwa. Yesu analankhula za kudzera mwa mayafera ochimwa.

Yesu anati:
“Mulungu anakonda kwambiri dziko mwakuti anapereka Mwana wake wobadwa yekha, kuti aliyense wokhulupirira Iye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha.”

Izi zikutanthauza
kuti aliyense amene
akhulupilira Yesu
amabadwa
m'banja
la Mulungu.

Mwina Nikodemo sanakhale wophunzira wa Yesu usiku umenewo. Koma patapita zaka zingapo, Nikodemo anasonyeza kuti ankakonda ndiponso kukhulupirira Yesu pothandiza m'manda Mwana wa Mulungu wopachikidwayo.

Zitatha izi, Yesu ndi ophunzira ake ananyamuka ulendo wa kumpoto. Anthu ena anafunikira kumva za Ufumu wa Mulungu, ndi kukhala ndi mwaŵi wokhulupirira Yesu wa ku Nazarete, Mwana wa Mulungu.

Mtsogoleri wa Kachisi Akuyendera Yesu

Nthano yochokera mu mau a Mulungu, Baibulo,

opezeka mu

Yohane 2-3, Numeri 21

"Polowela pa mau anu pamapasa kuwala."
Masalimo 119:130

Mapeto

Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu: Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi moyo. Chonde, lowani mmoyo mwanga ndikundi khululukira machimo anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse!
Johane 3:16